# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA MCHINJI M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi **La Nina wochepa mphamvu**. **La Nina** ndi kuzizira koposera mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific.

Boma la Mchinji likuyembekezereka kulandira mvula pa **mlingo wokhazikika komanso wochulukirapo**.


## October 2024




M'mwezi wa October, madera ambiri akuyembezereka kusalandira mvula.
Madera ena akuyembezereka kulandira mvula amlingo ochepela 20mm.

Mvulayi idzatsatana ndi mphepo yamkuntho komanso mphenzi.


## November 2024




Tiyembekezere mvula ya mlingo wokhazikika komanso wochepekerapo molinganizana ndi dzinja la 2023 ndi 2024. Madera ambiri a m'bomali ayembekezere kulandira m'mvula yamlingo wapakati pa 30mm ndi 80mm.


Mphepo yamkuntho ndi ziphaliwali zikuyembezereka kuchitik m'mbomali.

## December 2024





Dzinja likuyembekezereka kuyamba pakati pa sabata lomaliza la mwezi wa November ndi sabata lachiwiri la mwezi wa December 2024. Mvula ya mlingo wa pakati pa 200-250mm ikuyembekezereka kugwa mmadera a pa boma la Mchinji, TA's Mlonyeni, Dambe ndi Mavwere. Ena madera ozungulira TAs Mkanda ndi Zulu akuyembezereka kulandira mvula yamlingo wapakati pa 150-200mm.

## January 2025





Tiyembekezere mvula ya mlingo wokhazikika komanso wochulukirapo. Mvula ya mlingo wapakati pa 200 ndi 300mm ikuyembezereka kudzagwa madera ambiri a m'bomali. Madera ena a pa Mchinji Boma akuyembekezereka kulandira mvula yoposera mlingo wa 300mm.
Bomali liyembekezere kukhala ndi ng'amba yosaposera sabata imodzi madera ena.

## February 2025





Tiyembekezere mvula komanso wochulukirapo molinganizana ndi dzinja la 2023 ndi 2024. Madera ambiri ayembekezere kulandira mvula ya mlingo wa 180 ndi 250mm. Madera ozugulira TA Mkanda akuyembekezereka kudzalandira mvula yamlingo woposa 250mm. Ng'amba yosaposera sabata imodzi ikuyembekezereka madera ena m'bomali.

## March 2025




Madera ambiri a m'bomali ayembekezere kudzalandira mvula ya mlingo wa pakati pa 100 ndi 200mm. Madera ozungulira boma la Mchinji, TA Zulu, TA Mkanda ndi TA Mlonyeni akuyembekezereka kudzalandira mvula yochulukapo kuposa mlingo wa 200mm.
Madera ena dzinja litha kufika kumapeto sabata lomaliza la mweziwu.

## April 2025





Mwezi wa April ndikuyamba kutha kwamvula mdziko la Malawi.
Madera ambiri m'mboma la Mchinji akuyembekezereka kulandira mvula yamlingo wapakati pa 30-80mm.

Mvulayi omwe ndi mlingo wake wa mvula wokhazikika.

*Dzinja M'boma la Mchinji ikuyembekezereka kuyamba pakati pa sabata yomaliza ya mwezi wa November ndi sabata yachiwiri ya mwezi wa December 2024. Nyengoyi idzakhala itafika kumapeto pakati pa sabata yomaliza ya mwezi wa March ndi sabata yachiwiri ya mwezi wa April 2025. Chiyembekezo cha ng'amba yopitilira sabata imodzi ndi chachikulu m'bomali mwezi wa February ndi January. Dzinjali lidzatalika ndi masiku a pakati pa* ***110 ndi 140.***

| MCHINJI | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 6.7 | 21.4 | 13.0 |
| NOV | 42.7 | 102.4 | 109.3 |
| DEC | 175.6 | 274.0 | 245.2 |
| JAN | 235.9 | 298.1 | 317.3 |
| FEB | 174.5 | 236.0 | 219.2 |
| MAR | 111.5 | 217.0 | 192.1 |
| APR | 33.5 | 82.9 | 68.3 |





**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**
**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: